
UTHENGA WA MTANDA
Phunziro 2, July 11, 2026


"Pakuti uthenga wa mtanda ndi
chopusa kwa iwo amene
akuwonongeka, koma kwa ife amene
tikupulumutsidwa uthengawu ndi
mphamvu ya Mulungu. "
(1 Akorinto1:18, CCL)

1 Akorinto 1:17-31 ikunena za mmene mtanda umakhudzira miyoyo ya anthu.

Kwa okhulupirira, mtanda ndi chizindikiro cha chipulumutso. Koma kwa anthu omwe anakhalapo m'zaka zana loyamba, mtandawo unkaimira imfa yochititsa manyazi ya munthu olakwa.

Kupulumutsidwa ndi munthu amene anafera pa mtanda n’kuukanso? Kwa anthu, zimenezi zimaoneka ngati zopusa, zopanda nzeru, komanso zofooka. Koma kwa ifeyo omwe tatsegula mitima yathu ku maitanidwe a Mzimu Woyera, mtanda ndi “mphamvu ya Mulungu, [...] nzeru, chilungamo, chiyeretso, komanso chiombolo” (1 Akorinto 1:18, 30).







- Nzeru za Mulungu
- Misala ya Mtanda
- Mphamvu ya Mulungu
- Uthenga wa Mtanda
- Kupusa ndi Kufooka kwa Mulungu

# NZERU ZA MULUNGU



"Koma kwa iwo amene Mulungu anawayitana, Ayuda ndi Agriki omwe, Khristu ndi mphamvu ya Mulungu ndi nzeru za Mulungu. " (1 Akorinto 1:24)



Ku Atene, Paulo anayesetsa kukopa anthu anzeru pogwiritsa ntchito nzeru za anthu. Koma kuyambira pamenepo, anatsimikiza mtima kugwiritsa ntchito nzeru za Mulungu zokha.

Mulungu mwiniwake anamutuma kukalalikira uthenga Wake "osati ndi mawu a nzeru za anthu, kuti mtanda wa Khristu usataye mphamvu yake" (1 Akorinto 1:17).

Kodi nzeru ya Mulungu imene Paulo analalikira ndi yotani?



Nzeru za Mulungu zimawononga 'nzeru za anzeru'; zimachotsa 'kumvetsetsa kwa ozindikira' (1 Akorinto 1:19); ndipo 'zimachititsa nzeru za dziko kukhala zopusa' (1 Akorinto 1:20).

Mosiyana ndi mmene anthu amaganizira, nzeru za Mulungu zili mukupulumutsa okhulupirira kudzera mu "kupusa kwa ulaliki" (1 Akorinto 1:21).

# MISALA YA MTANDA

"koma ife timalalikira Khristu wopachikidwa. Chitsa chokhumudwitsa kwa Ayuda ndi chopusa kwa a mitundu ina." (1 Akorinto1:23)



Mawu achigriki akuti *mōria* (misala, kupusa, uchitsiru) amagwiritsidwa ntchito kasanu m'buku la 1 Akorinto.

- "Uthenga wa mtanda ndi chopusa kwa iwo amene akuwonongeka" (1 Akorinto 1:18)
- "Mulungu amakondweretsedwa kuti kudzera mu chopusa cha zomwe zinalalikidwa apulumutse iwo amene akhulupirira" (1 Akorinto 1:21)
- "Khristu wopachikidwa, [...] ndi chopusa kwa a mitundu ina" (1 Akorinto 1:23)
- "Kwa munthu mwachibadibwe [...] zinthu za Mzimu wa Mulungu [...] ndi zopusa" (1 Akorinto 2:14)
- "Pakuti nzeru ya dziko ndi yopusa pamaso pa Mulungu" (1 Akorinto 3:19)



Mtanda ndi chinthu chopusa kwa anthu otayika; kwa iwo amene sadziwa Mulungu (amitundu ina); kwa iwo amene amangoganizira za dziko lapansi lino; ndi kwa iwo amene amatsogoleredwa ndi nzeru zawo zokha.

Koma mtanda ndi dalitso kwa amene akupulumutsidwa, ndiye kuti, kwa amene ali ofunitsitsa kuona mtanda mmene Mulungu amawuonera.

# MPHAMVU YA MULUNGU

"Pakuti uthenga wa mtanda ndi chopusa kwa iwo amene akuwonongeka, koma kwa ife amene tikupulumutsidwa uthengawu ndi mphamvu ya Mulungu." (1 Akorinto 1:18)

Mtanda uli ndi mphamvu yowonetsa kuipa koopsa kwa munthu ndi ubwino waukulu wa Mulungu (1 Akorinto 1:18).

| Khalidwe loipa kwambiri la munthu | Ubwino waukulu wa Mulungu |
| --- | --- |
| Misala | Mphamvu |
| Kukana | Kuvomereza |
| Kudziononga | Kukhululukira |
| Chionongeko | Chipulumutso |

Anthu amene amakana mtanda amakolola zotsatira za zochita zawo zoipa, ndipo potsirizira pake adzawonongedwa ndi Iye amene anamukana.

Mphamvu ya Mulungu, imene inaonetsedwa pa mtanda, imatha kuyanjanitsa munthu ndi Mulungu pomukhululukira machimo ake onse, ndi kumupatsa moyo wosatha(Akolose 1:20; 1 Petro 2:24).



# UTHENGA WA MTANDA

"Tsono poti mwa nzeru za Mulungu dziko lapansi mu nzeru zake silinamudziwe Iye, Mulungu amakondweretsedwa kuti kudzera mu chopusa cha zomwe zinalalikidwa apulumutse iwo amene akhulupirira.
(1 Akorinto 1:21)





**Ndichifukwa chiyani kulalikira uthenga wa mtanda kumaonedwa ngati kupusa (1 Akorinto 1:21-24)?**

**Ayuda amayembekezera Mesiya amene adzawamasula ku ulamuliro wopondereza wa Aroma. Pamene Yesu analengeza kuti apachikidwa pamtanda, ophunzira ake anachita mantha kwambiri. Kuwonjezera pamenepo, kwa Myuda, munthu wopachikidwa pamtengo ankawonedwa ngati wotemberereredwa ndi Mulungu (Deuteronomo 21:23). Kwa anthu a mitundu ina, omwe sankayembekezera ngakhale pang'ono Mumpulumutsi, chigamulo chake chinali chomwecho: mtanda ndi kupusa.**

**Koma kwa angelo, uthenga wa pamtanda unali chinthu chosiyana kwambiri. Yesu, yemwe ankamudziwa Kumwamba, adalola kuphedwa chifukwa cha chikondi pa mbadwo womwe udamukana. Limeneli ndilo lingaliro limene Paulo ankafuna kupereka kudzera m'kulalikira kwake.**

**Uthenga wa pamtanda ukuwonetsa momwe Mulungu adalolera kufikira kuti atipatse chipulumutso.**

# KUPUSA NDI KUFOOKA KWA MULUNGU

"Pakuti za Mulungu zooneka ngati zopusa, ndi za nzeru kuposa nzeru za munthu, ndipo za Mulungu zooneka ngati zofowoka, zili ndi mphamvu kuposa mphamvu za munthu.." (1 Akorinto 1:25)



Kodi Mulungu ali wopusa kapena wofooka mwanjira ina iliyonse? (1 Ako. 1:25)?

Ayi ndithu, chifukwa Mulungu alibe zofooka zilizonse. Paulo akungogwiritsa ntchito fanizo: Ankatanthauza kuti ngati Mulungu akanakhala ndi maganizo amene anthu angaone ngati opusa, akanakhalabe anzeru kuposa maganizo anzeru kwambiri a munthu. Ndipo ngati Mulungu akanakhala ndi chimene anthu angachione ngati kufooka, chikanakhalabe champhamvu kuposa mphamvu zazikulu kwambiri za munthu.



Nzeru zonse zimene anzeru kwambiri a dziko angasonkhanitse sizingathe kupanga kapena kulingalira ndodomeko ya chipulumutso cha anthu.

Ndi Mulungu yekha amene wakwanitsa kupereka chiombolo, kudzera mu mphamvu ya nsembe ya Yesu yoperekedwa pamtanda, kwa "iwo amene akupulumutsidwa" (1 Akorinto 1:18); kwa "okhulupirira" (1 Akorinto 1:21); ndi kwa "iwo amene anaitanidwa" (1 Akorinto 1:24).

Dziwani kuti ndi okhawo amene amakhulupirira Yesu povomera kuyitanidwa kwa Mzimu Woyera amene adzapulumutsidwe.



“Kwa anthu ambiri a masiku ano, mtanda wa Kalvare wazunguliridwa ndi zikumbukiro zopatulika. Malo amene Khristu anapachikidwapo ali ndi tanthauzo lopatulika. Koma m’nthawi ya Paulo, mtanda unkaonedwa ngati chinthu chochititsa kunyansidwa ndi mantha. Kulalikira kuti Mpulumutsi wa anthu onse ndi munthu amene anafera pa mtanda kunali chinthu chimene mwachibadwa chinkabweretsa kunyozedwa ndi kutsutsidwa. […]

Anthu akanamuona Paulo ngati munthu wopanda nzeru chifukwa choyesera kufotokoza kuti mtanda ungakhale bwanji wokhudzana ndi kukwezedwa kwa anthu kapena chipulumutso cha anthu.

Koma kwa Paulo, mtanda ndiwo unali chinthu chofunika kwambiri kuposa china chilichonse. […] Iye ankadziwa kuchokera pa zimene anakumana nazo yekha kuti pamene wochimwa waona chikondi cha Atate, chimene chaonekera mu nsembe ya Mwana wake, ndipo wavomera kutsogoleredwa ndi mphamvu ya Mulungu, mtima wake umasandulika, ndipo kuyambira pamenepo, Khristu amakhala zonse pa moyo wake."

EGW (The Acts of the Apostles, p. 245)